

Level 2

# Dotolo wa Thonje

Author: Michelle Matthews
Illustrator: Jean de Wet
Translator: Agnes N.Singine Nyendwa



Nthawi ina, muzaka 200, kunali munthu wina dzina lake Margaret Ann Bulkly. Margaret anali kukhala m'dziko lozizizilira, malo amsipu otchedwa Ireland, m'dziko la Great Britain.

Margaret anali wochenjera ndipo wofuna kudziwa zinthu. Margaret anali ndi maloto a akulu. Margaret anali wolimba mtima ndipo anali kuchita ndeu ndi anthu ngati zinthu sizidamyendere bwino.



Amai ndi atate a Margaret analipira ndalama za maphunziro a mlongosi wake kuti akakhale loya. Ndi kugwiritsa nchito ndalama zidakhala kuti mlongosi wake amange chikwati ndi mwana wa bambo wina wolemera kwambiri.
Margaret anali wochenjera ndipo anali ndi maloto a akulu kwambiri. Koma kunalibe ndalama zakuti aphunzire, ngakhale maphunziro a osunga ana kapena a unamwino.
Margaret anali wolimbika. "Ndifuna kukhala dotolo!" anati. Koma zaka 200 zapitazi, mtsikana sanali kuloledwa kukhala loya kapena wandale kapena dotolo.



Margaret anali ndi amalume ake amene anali otchuka pa za kujambula ndi utoto. Dzina lao linali James Barry.
M'modzi mwa abwenzi a James Barry anali a General Miranda ochokera ku Venezuela. A General Miranda anali ndi chipinda momwe anali kusungira mabuku - chinali chabwino ndiponso chachikulu kwambiri.
M 'chipindamo munali mabuku ambiri kupyora pa 6000!
Ndifuna kuwerenga iyi! Ndi iyi! Ndi iyi!" ananena Margaret.
Margaret anali wochenjera ndi kufunitsitsa kudziwa zinthu.
General Miranda anasilira.



Pamene amalume ake a Margaret a James Barry anamwalira, anamsiyira ndalama. "Zinali ndalama zokwanira kuti angathe kuphunzira za udotolo!" ananena General Miranda.
"Koma sindingakhale dotolo," Margaret anati.
"Mnyamata angathe kukhala dotolo," ananena General Miranda. "Ndipo ungathe kubvala zobvala ngati mnyamata."
Margaret anali wolimbika ndipo anali kutsata zimene anali kukhulupilira. Anali kufunitsitsa kukhala dotolo. Tero anameta tsitsi lake. Anaphunzira kulankhula ngati munthu wamwamuna. Anabvala zobvala zachimuna. Kuchokera apo, anthu onse sanadziwe kuti Margaret anali munthu wachimai.

Anakhala James Barry, ngati amalume ake.



Jame Barry anali wolimbika pa kuphunzira za mankhwala. Anali kupunzira mizati khumi ndi itatu ndipo anaphunzira munthawi ya mafundi yonse pamene ena anapita ku chuti. Patapita zaka zisanu, sakadalemba mayeso ake otsiriza? Opangitsa mayeso anaganiza kuti ndi mwana wachichepere! James Barry sanali ndi ndebvu chifukwa sanali munthu wamwamuna.



Dr. James Barry anali wolimba mtima ndipo anali ofunitsitsa kudziwa zinthu. Dr. James Barry anali ndi maloto a akulu. Tero anakakhala m'modzi wa a gulu la nkhondo. Mugululi, ungathe kuona dziko la pansi.
Mu chaka cha 1816, gululi linatumiza Dr. James Barry kupita ku Cape Town. Cape Town unali mzinda waung'ono, mzinda umene uli ku South Africa wosangalatsa. South Africa inali kutali ndi Ireland.
Dr. James Barry ankondwera.



Dr. James Barry anali wamfupi ndiponso woonda. Anali kubvala makokolo kuti azioneka wamtali ndi kuika zinthu zakuti zobvala zizioneka zazikulu.
Anthu a ku Cape Town anaitana Dr. James Barry a kapok dokter, dotolo wa thonje.



"Ndingafunitsitse kukudula makutu!" Dr. James Barry anali kuzazira aliyense amene anam'bechera.
Nthawi ina Dr. James Barry anawomberana mfuti ndi munthu wina! Mwa mwai wanji onse awiri sanalasidwe.
Kodi ndi chiyani adotolo anali kukonda zandeu? Margaret anali wolimba mtima koma analinso wamantha.
Anali kudziwa kuti ngati wina wake wazindikira kuti ndiye anali Dr. James Barry sadzaloledwanso kukhala dotolo.
Aliyense ayenekera kukhulupilira kuti Dr. James Barry anali munthu wamwamuna.



Dr. James Barry anali kuchita ndeu ngati waganizira kuti chinthu sichilibwino.
Mu Cape Town, anthu odwala makate anali kuwasamula kupita ku Robben Island. Akhatewo anali kuwapereka ku chisumbu chifukwa anthu anakhulupilira kuti angatenge matendawo mosabvuta.
Nyumba za donthi ndi zakudya zoipa zinali kupanga amakatewo kudwala kwambiri.
Dr. James Barry pempha atsogoleri a Cape Town  kuti apereke mkhalidwe wa udongo ndi zakudya zabwino kwa anthu odwala ku Robben Island.



Zaka zapita, Dr. James Barry anagwira nchito ku chipatala cha a nkhondo.
Uku anakomana ndi Florence Nightingale, m'namwino.
Florence Nightingale anali kudziwika kuti ndi mai wa nyale, chifukwa anali kuona ankhondo ovulala nthawi ya usiku.
Anakhala otchuka nthawi ya nkhondo chifukwa anapempha mkhalidwe wa ukhondo ndi zakudya zathanzi za ankhondo kwa atsogoleri a ankhondo.
Kwa zaka zambiri a Dr. James Barry anali kupempha zimodzimodzi.



Dr. James Barry anayenda m'maiko osiyanasiyana. Anagwira nchito mu South Africa, St. Helena, Barbados, Mauritius, Trinidad and Tobago, Malta, Corfu, Jamaica, Crimea, West Indies, Canada... malo11.

Ulendo wosangalatsa kwambiri.



Anthu sanazindikire kuti Dr. James Barry anali munthu wa chimai mpaka atamwalira mchaka cha1865.
Mchaka chimenecho, Dr. Elizabeth Garret Anderson anakhala dotolo wachimai woyamba mu Great Britain.
Dr. James Barry wationetsa kuti atsikana angathe kuchita chinthu chilichonse chimene amafuna kuchita.





This book was made possible by Pratham Books' StoryWeaver platform. Content under Creative Commons licenses can be downloaded, translated and can even be used to create new stories - provided you give appropriate credit, and indicate if changes were made. To know more about this, and the full terms of use and attribution, please visit the following link .
Story Attribution:
This story:Dotolo wa Thonjeis translated byAgnes N.Singine Nyendwa. The © for this translation lies with Agnes N.Singine Nyendwa, 2019. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license. Based on Original story:'The Cottonwool Doctor', byMichelle Matthews. © Book Dash , 2014. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.
Images Attributions:
Cover page:Man looking at us, byJean de Wet© Book Dash, 2014. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 2:Man and woman fighting with sticks, byJean de Wet© Book Dash, 2014. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 3:Woman bandaging a teddy bear, byJean de Wet© Book Dash, 2014. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license. Page 4:Woman climbing a ladder at the library, byJean de Wet© Book Dash, 2014. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 5:Man holding a coat on a hanger, byJean de Wet© Book Dash, 2014. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 6:Man writing with quill, byJean de Wet© Book Dash, 2014. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 7:Man pointing at Africa on a map, byJean de Wet© Book Dash, 2014. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 8:Man sitting by a window, byJean de Wet© Book Dash, 2014. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 9:Woman shooting at something, byJean de Wet© Book Dash, 2014. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 10:People standing at the shore, byJean de Wet© Book Dash, 2014. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Disclaimer:https://www.storyweaver.org.in/terms_and_conditions

Some rights reserved. This book is CC--BY--4.0 licensed. You can copy, modify, distribute and perform the work, even for commercial purposes, all without asking permission. For full terms of use and attribution, http://creativecommons.org/licenses/by/4.0/

This book was made possible by Pratham Books' StoryWeaver platform. Content under Creative Commons licenses can be downloaded, translated and can even be used to create new stories - provided you give appropriate credit, and indicate if changes were made. To know more about this, and the full terms of use and attribution, please visit the following link .
Images Attributions:
Page 11:Woman holding a lantern, byJean de Wet© Book Dash, 2014. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 12:Ship sailing in the seas, byJean de Wet© Book Dash, 2014. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 13:Pictures of a man and a woman, byJean de Wet© Book Dash, 2014. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 14:A top hat, byJean de Wet© Book Dash, 2014. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Page 15:Lots of teddy bears, byJean de Wet© Book Dash, 2014. Some rights reserved. Released under CC BY 4.0 license.Disclaimer:https://www.storyweaver.org.in/terms_and_conditions

Some rights reserved. This book is CC--BY--4.0 licensed. You can copy, modify, distribute and perform the work, even for commercial purposes, all without asking permission. For full terms of use and attribution, http://creativecommons.org/licenses/by/4.0/

Dotolo wa Thonje (Chinyanja)

Margaret anali wofunitsitsa kudziwa zinthu. Margaret anali ndi maloto akulu. Koma zaka 200 zitapita, mtsikana sanali kuloledwa kukhal dotolo. Teo anameta tsitsi lake ndi kubvala zobzala za munthu wa mwamuna. Kuchokera pamenepo, anthu sanadziwe kuti Margaret ndi munthu wachimai. Anakhala James Barry.

This is a Level 2 book for children who recognize familiar words and can read new words with help.

PRATHAM BOOKS storyweaver

Pratham Books goes digital to weave a whole new chapter in the realm of multilingual children's stories. Knitting together children, authors, illustrators and publishers. Folding in teachers, and translators. To create a rich fabric of openly licensed multilingual stories for the children of India -- and the world. Our unique online platform, StoryWeaver, is a playground where children, parents, teachers and librarians can get creative. Come, start weaving today, and help us get a book in every child's hand!